

Kodi Mumachita Zinthu Moona Mtima?

Onani ubwino wochita zinthu moona mtima ndiponso kuipa kochita zinthu mosaona mtima.



1

Ndikupita kuphwando. Mayi kapena bambo akadzakufunsa mawa, udzangowauza kuti sindinachoke.

KODI MUNGATANI?

Kuchita zimene mkulu wanu wakuuzani.
 Ngati makolo anu atakufunsa zinazake, ungowanamiza kuti uteteze mchimwene wako.

Muuzeni mchimwene wanu kuti simunganene zabodza kuti mumuteteze. Ngati mchimwene wako angachoke kupita kwina kwake, uyenera kuwauza makolo ako.

Pangakhale zotsatira zoipa ngati makolo atazindikira kuti tawanamiza:

Zinthu zabwino zimene zingachitike ngati mutauza makolo anu zoonā:

“Makolo anu azidzakukhulupirani kwambiri ngati mumawauza zoonā.”



—Natasha.

(Werengani Salimo 119:163. Ganizirani mmene inuyo mumamvera anthu akamanena zabodza komonso kuchita zachinyengo.)

2

Ndachita chinthu choipa kwambiri ndipo chikumbumtima changa chikundivutitsa.



KODI MUNGATANI?

Kungobisa zimene mwachitazo.

Kuuza makolo anu kapena Mkhristu wodziwa zambiri.

Kuipa kobisa zimene tachita:

Ubwino wouza ena zimene tachita:

“Ngati tabisa zoipa zimene tachita, sitingakhale ndi chikumbumtima chabwino ndipo zimenezi zingapangitse kuti tisamasangalale. Kuwonjezera pamene, nkhaniyo ikadziwika zinthu zimaipa kwambiri.”



—Carly.

(Werengani Mlaliki 12:14 ndi Yakobo 5:14-16. Ganizirani mmene mungasangalalire ngati mutaulula zimene mwachita kenako n’kuthandizidwa.)

3

Iwe,
tandiuzireko
yankho la
funso ili!



KODI MUNGATANI?

Kungolera, kuti musaoneke ngati mukudzilungamitsa.

Kumukanira, zilibe kanthu kuti akuganizirani zotani.

Kuipa kouzira mnzanu mayeso:

Ubwino wokana kuuzira mnzanu mayeso:

“Munthu akayamba kuchita zinthu mosaona mtima amazolowera khalidwe loipali ndipo saona vuto lililonse akamachita zinthu mosaona mtima.”



—Karen.



(Werengani Miyambo 29:25. Ganizirani mmene mungasangalalire chifukwa chodziwa kuti mwayesetsa kuchita zinthu zoyenera.)

Tsopano ganizirani chitsanzo cha zinthu zimene zingakupangitseni kuchita zinthu mosaona mtima. Kenako lembani zinthu zabwino zimene zingachitike ngati mutasankha kuchita zinthu moona mtima ndiponso zoipa zimene zingachitike ngati mungachite zinthu mosaona mtima.

CHITSANZO:

ZIMENE MUKANACHITA:

ZIMENE MUKUYENERA KUCHITA:



ZOTSATIRA ZAKE

Zoipa:

Zabwino:

Mfundo yofunika kuikumbukira: Zimene mumachita pa nkhani ya kuona mtima zimasonyeza khalidwe lanu. Choncho dzifunseni kuti: 'Kodi ndikufuna kuti anthu azindidziwa kuti ndine munthu wotani? Kodi ineyo ndikufuna kukhala munthu wotani?'—Miyambo 20:11.